zabwino kwambiri.

-Pachiyambi, kunalibe minga.
-Pachiyambi, kunalibe udzu.
-Pachiyambi, chimanga chonse chimkamera bwino kwambiri.

-Mulungu analenga zithu zonse zabwino kwambiri chifukwa chakuti amatikonda kwambiri.



PHUNZIRO LA 6

1. Kodi chiyambi ndi chiyani?
-Pachiyambi ndi nthaŵi yayitali yapitayo yimene Mulungu analenga chinthu china chilichose.

2. Pachiyambi, kodi ndi ndani amene analenga zinthu zonse zimene zili pa dziko la pasi?
-Mulungu.

3. Kodi pa dziko la pasi panali chiyani Mulungu asanalenge chinthu china chilichose?
-Palibe.

4. Kodi nanga ngati panalibe chinthu china chilichose pa dziko la pasi , Mulungu anagwiritsa ntchito chiyani polenga zinthu zonse?
-Palibe.

5. Kodi nanga Mulungu analenga bwanji dziko la pasi?
-Mulungu analenga dziko la pasi posagwiritsa nchito chinthu china chilichose.

6. Kodi Mulungu anatha bwanji kulenga zinthu zonsezi popanda kugwiritsa nthito chinthu china chilichose?
-Mulungu ndi wamphamvu zonse.
-Mphamvu ya Mulungu siyitha.
-Mphamvu ya Mulungu ndi yampaka kalekale.

7. Kodi mphamvu ya Mulungu yili ndi malile?
-Iyayi.

8. Kodi Satana, ziwanda zake ngakhalenso anthu ali ndi mphamvu zambiri kuposa Mulungu?
-Iyayi.

9. Kodi panali amene anamuphunzitsa Mulungu malengedwe a zinthu zonsezi?
-Palibe.

10. Kodi ndi chifukwa chiyani palibe amene anamuphunzitsa Mulungu?
-Pachiyambi panalibe wina aliyense amene anakatha kumuphunzitsa Mulungu.
-Kupatula chifukwa chimenechi, Mulungu samafuna wina aliyense kuti amuphunzitse Iye.

11. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu samafuna wina aliyense kuti amuphunzitse Iye?
-Chifukwa chakuti Mulungu amadziwa zonse.
-Chifukwa chakuti nzeru za Mulungu sizitha.
-Chifukwa chakuti nzeru za Mulungu ndi zampaka kalekale.

12. Kodi satana ndi ziwanda zake ngakhale anthu amadziwa zonse ngati mmene amadziwila Mulungu?
-Iyayi.
-Mulungu yekha ndi amene amadziwa zonse.

-Pachiyambi, Mulungu analenga kumwamba ndi dziko la pasi.

-Tiyeni tiŵerenge za mmene linalili dziko la pasi Mulungu asanalenge chinthu chilichonse.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:1-2a

1-Pachiyambi Mulungu, analenga kumwamba ndi dziko la pasi.
2-Dziko la pasi linali lopanda mawonekedwe enieni ndipo munalibe china chilichonse, mdima unali utaphimba nyanja yayikulu ponseponse.



-Kodi kunali kuvuta kwa Mulungu kulenga somba ndi mbalame zonse?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Mulungu ndi wa mphamvu zonse.
-Palibe chinthu china chilichonse chimene angalephere kuchichita Mulungu.

-Kodi Mulungu analenga somba ndi mbalame zosiyanasiyana za mitundu yingati?
-Yambiri, palibe amene angathe kuyiŵerenga.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu analenga somba ndi mbalame zonse?
-Kodi Mulungu amafuna somba ndi mbalame kuti akhale?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anamulengela ndani somba ndi mbalame zonse?
-Mulungu anaŵalengela anthu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu analenga somba ndi mbalame zonse?
-Chifukwa chakuti Mulungu amaŵakonda anthu kwambiri.

-Kodi Mulungu anati chiyani pa zinthu zonse zimene Iye anazilenga?
-Mulungu anati kuti zonse zinali zabwino.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anatha kulenga zinthu zonse zabwino kwambiri?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri.

-Zinthu zonse zimene Mulungu anazilenga pachiyambi zinali

18-kuti idziŵala usana ndi usiku, kulekanitsa kuyera ndi mdima. Ndipo anawona kuti zinali zabwino.
19-Ndipo kunada, ndiponso kunacha. Ili linali tsiku lachinayi.

-Pa tsiku lachinayi, Mulungu analenga dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi.

-Kodi Mulungu analenga bwanji dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi?
-Pangolankhula.
-kodi chifukwa chiyani dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi sizigwa mu mlengalenge?

-Chifukwa chakuti Mulungu anazisiya kumeneko.
-Chifukwa chakuti ntchito ya Mulungu ndi yabwino kwambiri.

-Kodi Mulungu analenga chiyani pa tsiku lachisano?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:20-21 ndi 23

20-Zitatero Mulungu adatinso, "M'nyanja mukhale za moyo zosiyanasiyana zambiri, ndipo pakhalenso mbalame zowuluka mu mlengalenga."
21-Chomcho Mlungu analenga somba zazikuruzikuru za mnyanja, pamodzi ndi zolengedwa zina zonse zokhala m'madzi, ndiponso mbalame zowuluka za mitundumitundu ndiponso Mulungu anaziwona zonse zimene anazilengazo kuti zinali zabwino.
23-Ndipo kunada, ndiponso kunacha. Ili linali tsiku lachisano.

-Pa tsiku lachisanu, Mulungu analenga somba ndi mbalame zonse.

-Kodi Mulungu analenga bwanji somba ndi mbalame zonse?
-Pongolakhula.



-Kodi dziko la pasi linali lotani Mulungu asanalilenge?

-Pachiyambi, kunalibe kuwala.
-Pachiyambi, mdima unaphimba dziko lonse la pasi.

-Kodi munakakhala osangalala kunakakhala kulibe kuwala kwa dzuwa masana?
-Iyayi.

-Kodi munakakhala osangalala kunakakhala kulibe kuwala kwa mwezi usiku?
-Iyayi.

-Kodi panakakhala powophysa kwambiri pa dziko la pasi panakakhala kuti palibe kuwala?
-Inde.

-Sibwezi mukutha kuwona podzala mbewu zanu.
-Sibwezi mukutha kuwona pomanga nyumba zanu.
-Sibwezi mukutha kuwonana.

-Pachiyambi, panalibe kuwala.
-Pachiyambi,  panalibe ntunda.
-Pachiyambi, madzi anaphimba dziko lonse la pasi.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:2b

2-Mdima unali utaphimba nyanja yayikulu ponseponse, ndipo Mzimu wa Mulungu umkayendayenda pamwamba pa madziwo.

-Pachiyambi, panalibe moyo pa dziko la pasi.
-Koma Mulungu Mzimu Woyera analipo.

-Mulungu Mzimu Woyera amkadikilira kuti ayambe ntchito yake yolenga china chilichonse.

- Kodi mukukumbukira kuti pali Mulungu mmodzi yekha, koma pali Anthu atatu amene ali Mulungu mmodziyo?

-Mulungu Atate, Mulungu Mwana (Mpulumutsi), ndi Mulungu Mzimu woyera analenga zinthu zonse pamodzi.

-Pachiyambi, kodi Mulungu analenga chiyani pa tsiku loyamba?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:3

3-Ndipo Mulungu anati, "kuyere," ndipo kudayeradi.

-Pa tsiku loyamba, Mulungu analenga kuwala.

-Kodi Mulungu analenga bwanji kuwala?
-Mulungu analenga kuwala Kungolankhula.

-Kodi pali amene angathe kulenga kuwala pongolakhula?
-Palibe.

-Apa pali chitsanzo:

-Tsiku lina usiku, mwapita kutchile kuli mdima.

-Kulibe kuwala kwa mwezi ngakhalenso kuwala kwa nyenyezi.
-Kuli mdima wambiri, ndipo simungathe kuchiwona chinthu china chilichonse.
-Kodi mungathe kungolankhula kuti, "kukhale kuwala", ndipo kuwalako ndikubweradi?
-Iyayi.
- Kodi Mulungu anadziwa bwanji kulenga kuwala?

-Mulungu amadziwa zonse.



-Yambiri, palibe amene angathe kuŵerenga.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu analenga zomera ndi mitengo yonseyi?
-Kodi Mulungu amafuna zomera ndi mitengo kuti akhale?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anaŵalengela ndani zomera ndi mitengo yonseyi?
-Mulungu anaŵalengela anthu.

- Kodi chifukwa chiyani Mulungu analenga zomera ndi mitengo yonseyi?
-Chifukwa chakuti Mulungu amaŵakonda anthu kwambiri.

-Kodi kunakakhala kuti kulibe mitengo, munakatha kumanga nyumba?
-Iyayi.
-Mulungu anatilengela ife mitemgo chifukwa chakuti amatikonda.

-Kodi kunakakhala kuti kulibe zakudya, bwenzi mukudya chiyani?
-Palibe.
-Mulungu anatilengela zakudya chifukwa chakuti amatikonda.

-Kodi Mulungu analenga chiyani pa tsiku lachinayi?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:16-19

16-Mulungu analenga miyuni iŵiri yayikuru: dzuŵa loŵala masana , ndipo mwezi woŵala usiku. Adalenganso nyenyezi .
17-Mulungu anayika miyuniyo mu mlengalenga, kuti idziwunikira dziko la pasi,

-Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu yekha ndi amene angathe kuŵalamulira madzi kuti asendere mmbuyo, ndipo madziwo ndikumvera?

-Chifukwa chakuti ndi Mulungu amene analenga madzi.

-Kodi china ndi chiyani chimene Mulungu analenga pa tsiku lachitatu?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:11-13

11-Keneko Mulungu adati, "Pa nthaka pamere zomera zobala njere, ndiponso mitengo yobala zipatso za njere malinga ndi mtundu wakwe," Ndipo zinachitikadi.
12-Motero pa nthaka panamera zomera za mitundu yonse, zipatso zokhala ndi njere ndi mitengo yobereka zipatso za njere malingana ndi mitundu yake. Mulungu anawona kuti zinali zabwino.
13-Ndipo kunada, ndiponso kunacha. Ili linali tsiku lachitatu.

-Kodi Mulungu analenga bwanji zomera zonse ndi mitengo?
-Kungolankhula.

-Kodi kunali kovuta kwa Mulungu kulenga zomera zonse ndi mitengo?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Mulungu ndi wa mphamvu zonse.
-Palibe chinthu china chilichonse chimene Mulungu sangathe kuchichita.

-Kodi Mulungu analenga mitundu yosiyanasiyana ya zomera ndi mitengo yingati?



-Palibe china chilichonse chimene Mulungu samachidziwa.

-Kodi kunali kovuta kwa Mulungu kulenga kuwala?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Mulungu ndi wamphamvu zonse.
-Palibe chimene Mulungu angarephere kuchita.

-Kodi Mulungu anaganiza chiyani za kuwala kumene Iye anakulenga?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:4a

4-Mulungu adawona kuti kuwalako kunali kwabwino.

-Kuwala kumene Mulungu anakulenga kunali kwabwino.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri.
-Zinthu zonse zimene Mulungu amachita zimakhala zabwino kwambiri.

-Amuna amamanga nyumba koma nthaŵi zina denga limadontha.
-Akazi amawumba miphika koma nthaŵi zina miphikayo imasweka.
-Koma Mulungu analenga zinthu zonse zabwino kwambiri.
-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri.

-Kodi Mulungu anachita chiyani atatha kulenga kuwala?

Tiyeni tiŵerenge 1:4b-5

4-Mulungu adakulekanitsa kuyerako ndi mdima.
5-Mulungu anakutcha kuwalako kuti "masana," ndipo mdimawo Iye anawutcha kuti "usiku." Ndipo kunada, ndi

kucha, ili linali tsiku loyamba.

-Pamene Mulungu analenga kuwala, Mulungu sanawuchotse mdima onse.

-Mulungu anawusiya mdima wina pa dziko la pasi kuti idzikhala nthaŵi ya usiku.

-Kodi kunakhala bwanji Mulungu anakakhala kuti sanasiye mdima wina pa dziko la pasi?
-Sibwenzi tikugona.

-Mulungu anasiya mdima wina pa dziko la pasi kuti tidzitha kugona.
-Zonse zimene Mulungu amachita zimakhala zabwino kwambiri.

-Kodi Mulungu analenga chiyani pa tsiku lachiwiri?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:6-8

6-Kenaka Mulungu adati, "Pakhale chilekanitsa madzi, kuti madziwo akhale pa malo aŵiri alekana."
7-Choncho Mulungu analenga cholekanitsa madzi chija, naŵagaŵa madziwo, ena pasi pa cholekanitsacho ndipo ena pamwamba pake. Ndipo zinachitikadi chomcho.
8-Cholekanitsacho adachitcha dzila lakuti "Mlengalenga." Ndipo kunada, ndiponso kunacha, ili linali tsiku lachiŵiri.

-Patsiku lachiŵiri, Mulungu analenga mlengalenga.

-Kodi Mulungu analenga bwanji mlengalenga?
-Kungolankhula.

-Kodi kunali kovuta kwa Mlungu kulenga mlengalenga?



-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wa mphamvu zonse.
-Palibe chinthu china chilichonse chimene sangathe kuchita Mulungu.

-Kodi Mulungu adaŵasiyanitsa bwanji madzi amene amene anaphimba dziko lonse la pasi?

-Mulungu adaŵayika madzi ena pamwamba pa mlengalenga kuchokera pa dziko la pasi.
-Mulungu anaŵasiya madzi ena onse otsala pa dziko la pasi.

-Kodi Mulungu analenga chiyani pa tsiku lachitatu?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:9-10

9-Mulungu adatinso, "Madzi a pa dziko la pasiŵa akhale pa malo amodzi, kuti pawoneke mtunda." Ndipo zinachitikadi.
10-Mulungu adawutcha mtundawo kuti "Dziko," ndipo madzi amene anaŵasonkhanitsa aja adaŵatcha kuti "Nyanja." Ndipo Mulungu adawona kuti zinali zabwino.

-Pa tsiku lachitatu, Mulungu adalenga mtunda.

-Pachiyambi, kunalibe mtunda.
-Pachiyambi, madzi anaphimba dziko la pasi lonse.

-Pa tsiku lachitatu, Mulungu anaŵalamura madzi kuti asendere mmbuyo kuti mtunda uwoneke.

-Kodi munthu atafika pa mtsinje, angathe kuwulamulira mtsinjewo kuti usendere mmbuyo kuti iye awoloke?
-Iyayi.